Kodi Tilidi ‘M’masiku Otsiriza’? (Gawo 2)

Nkhaniyi yachokera m’mutu 9 m’buku lakuti, *Kodi Baibulo Limaphunzitsa Chiyani Kwenikweni?* lomwe likupezeka pa jw.org/ny.

ZIMENE MUYENERA KUCHITA: Ganizirani mozama zimene mumakhulupirira ndiponso zifukwa zake, fufuzani zimene Baibulo limaphunzitsa, kenako ganizirani mmene mungafotokozere ena zimene mumakhulupirirazo.

KODI BAIBULO LIMANENA KUTI PALI ZINTHU ZINA ZABWINO ZIMENE ZIZICHITIKA ‘M’MASIKU OTSIRIZA’ ANO? —2 Timoteyo 3:1.

1 GANIZIRANI MOZAMA ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

N’chifukwa chiyani anthu ena angayankhe kuti ayi?

N’chifukwa chiyani ena angayankhe kuti inde?

Nanga **inuyo** mumakhulupirira zotani?

N’chifukwa chiyani mumakhulupirira zimenezi?

www.jw.org/ny © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

2 FUFUZANI ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA

Baibulo linaneneratu za zinthu zabwino zimene zidzachitike m’masiku otsiriza.
(Werengani mutu 9 m’buku lakuti, *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani,* ndime 12 mpaka 14.)

Werengani Danieli 12:4.

Kodi lembali likusonyeza bwanji kuti m’masiku otsiriza anthu a Mulungu adzadziwa zinthu zambiri zolondola?

Werengani Mateyu 24:3, 14 ndi Chivumbulutso 7:9.

Kodi ntchito yolalikira imene a Mboni za Yehova akugwira, ikukwaniritsa bwanji malembawa?

Masiku otsiriza akadzatha, Yehova adzachita zinthu zabwino zimene palibe munthu aliyense angakwanitse kuchita

www.jw.org/ny © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

Masiku otsiriza akadzatha zinthu zabwino zidzachitika.

(Werengani mutu 9 m'buku lakuti, *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani,* ndime 15 mpaka 18.)

Werengani 2 Atesalonika 1:6-9 ndi Chivumbulutso 21:3-5.

N'chifukwa chiyani tinganene kuti masiku otsiriza akadzatha, sipadzakhalanso mavuto?

Werengani Luka 21:34-36.

Kodi 'kukhala maso' kungatithandize bwanji m'masiku otsiriza ano?

Kodi ndi mfundo ziti zomwe zakulimbikitsani kwambiri?

www.jw.org/ny © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

3 FOTOKOZANI ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

WINA AKANENA KUTI . . .

Anthu adzawonongeratu dzikoli.

MUNGAYANKHE KUTI . . .

N'zoona kuti zinthu zikuoneka choncho, koma ndikukhulupirira kuti dzikoli siliwonongedwa chifukwa . . .

_____

_____

Kodi mungawerenge lemba liti kuti mumuthandize?

_____

Kodi mungafotokoze bwanji lembali pomuthandiza malinga ndi zimene amakhulupirirazo?

_____

WINA AKANENA KUTI . . .

Tikapitiriza kutulukira zinthu zatsopano zasayansi, kupanga zipangizo zamakono komanso mankhwala atsopano, tikhoza kuthetsa mavuto a m'dzikoli.

MUNGAYANKHE KUTI . . .

N'zoona kuti akatswiri akhala akutulukira ndiponso kupanga zinthu zatsopano. Koma posachedwapa Mulungu achita zinthu zabwino zimene *palibe* munthu aliyense angakwanitse kuchita. Mwachitsanzo, . . .

_____

Kodi mungawerenge lemba liti kuti mumuthandize?

_____

Kodi mungafotokoze bwanji lembali pomuthandiza malinga ndi zimene amakhulupirirazo?

_____

www.jw.org/ny © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania